

Zomwe mileme imadya

Zomwe tiphunzira sabata ino:

- Mitundu ya zakudya zomwe mileme imadya
- Momwe mileme imapezera chakudya chawo
- Za ekolokeshoni
- Zakudya zomwe mileme kumwera kwa Africa imadya

Phunziro

4



Moni anzanga, ndine Spike ndabwera kuti ndikuuzeni chinthu chimodzi chomwe ndimakonda - **CHAKUDYA!** Sizidzakudabwitsani kuti mitundu yosiyanasiyana ya mileme imadya zakudya zosiyanasiyana, koma zingakhale zodabwitsa kudziwa ndi zoti zakudya za mileme ndi zinthu ngati: tizilombo, zipatso, timadzi tomaluwa, mungu, nsomba, achule, abuluzi ang'onoang'ono ndi magari.

Chifukwa timadya zinthu zosiyanasiyana timapeza chakudya chatu m'njira zosiyanasiyana matupi athu amakhala ndi "mapangidwe" osiyanasiyana. Koma chinthu chimodzi chikhalabe chofanana; tonsefe timafunika kudya zakudya zambiri kuti tizitha kuuluka.

Mukawona chizindikiro ichi:



mufunika thandizo kuchokera kwa munthu wamkulu.

Musaiwale, chizindikiro cha pensulo chimatanthauza kuti ndi nthawi yanu yoti muchitepo kanthu!

Taphatikiza mawu onse atsopano pamndandanda wamawu kumapeto!




Mudzafunika:


- ✓ Pensulo
- ✓ Mapepala
- ✓ Mkasi
- ✓ mpango



Kwa inu!



Ntchito 1: Pezani chakudya:



Kodi mungapeze mitundu yonse ya zakudya zomwe mileme ingadye m'mawu ofufuzawa? Kumbukirani kufufuza chakumbuyo ndi kutsogolo, mbali, mmwamba ndi m'munsi, monga mmene mleme wanjala umasakira chakudya.



What bats eat

T	T	E	F	W	E	D	F	C	S	S	M	W	S
M	N	T	O	E	T	U	I	S	C	R	I	O	A
L	T	A	B	O	S	S	S	B	T	N	G	N	S
M	O	M	I	E	G	C	H	O	I	O	R	S	I
O	H	O	M	O	D	S	T	C	E	S	N	I	E
S	S	H	F	C	F	N	M	E	M	T	M	I	G
Q	S	L	R	T	L	A	F	S	S	B	A	F	E
U	H	U	B	T	O	B	O	W	D	F	S	Q	M
I	T	S	E	T	W	N	I	S	O	D	T	Q	R
T	O	R	E	U	E	E	S	G	O	G	I	E	F
O	M	E	T	F	R	C	F	O	L	H	U	T	S
S	C	O	L	S	S	T	F	R	B	F	R	S	O
T	N	C	E	F	N	A	S	F	E	E	F	C	N
E	O	U	S	N	E	R	M	T	M	S	O	N	U

- INSECTS
- NECTAR
- FRUIT
- FISH
- FROGS
- MOSQUITOS
- BEETLES
- FLOWERS
- BLOOD
- MOTHS




Play this puzzle online at : <https://thewordsearch.com/puzzle/3421819/>



1


Mitundu ya zakudya zomwe mileme imadya

Mileme yambiri imadya tizilombo ndipo imatchedwa "mainisekitivo". Zakudya zawo ndi zinthu ngati : kafadala, njenjete, udzudzu ndi ntchentche. Mileme yodya tizilombo ndi yaying'ono kwambiri kusiyana ndi mileme yomwe imadya zipatso, ili ndi maso aang'ono ndi mphuno zazifupi. Kodi mumadziwa kuti mileme yolembera 3-8g yokha (yofanana ndi ndalama zachitsulo) imatha kudya tizilombo 3000 usiku umodzi wokha? Mileme yodya tizilombo ndi yofunika kwambiri polimbana ndi tizirombo towonga m'munda ndi kuthandiza alimi kugwiritsa ntchito mankhwala ochepa ophera zilombo. Tangoganizani kuchuluka kwa udzudzu popanda ife mileme!



Popeza tizilombo ndi tating'ono kwambiri komanso tovuta kugwira, mileme yomweyodya tizilombo imagwiritsa ntchito njira yotchedwa **ekolokeshoni** kuti ipeze chakudya chawo. Zambiri za ekolokeshoni pambuyo pake....

"Ndimadya tizilombo tating'ono tambiri usiku uliwonse. Ndimasaka mumdima ndikuchipeza ndikudya chakudya changa ndikuwuluka. Ndiyenera kudya mwachangu chifukwa pakati pa kudya ndimakhala wotanganidwa ndikufuula kuti "ndikuwona" njira yanga mumdima



Mileme ina imakonda kudya zipatso ndipo imatchedwa "mafurugivo". Mileme yi imakonda kudya zipatso zofanana ndi zomwe anthu inu mumadya ndipo mileme yomwe imakonda zipatso zotsekemera imatha kukhala ndi mano owola! Mileme wodya zipatso amakhala ndi maso aakulu, mphuno zazitali (ndi mano amphamvu) zowathandiza kupeza ndi kudya chakudya chawo.

Kodi mumadziwa kuti njere za zipatsozo zimathera mu ndowe za mileme? Izi zitha kumveka ngati za umve koma ndizofunikira kwambiri, chifukwa iyi ndi njira yomwe mitengo yazipatso imakulira m'malo atsopano. Mileme yo imadya chipatsocho kenako n'kuulukira kwina kukadya kapena kukagona, mbewuyo n'kuiponya mu ndowe ndipo mitengo yatsopano ya zipatso imayamba kukula. Zabwino bwanji!



Moni, ndine Eidolon wamkulu. Mleme waukulu kwambiri wa zipatso kumwera kwa Africa. Maso anga akulu akulu komanso kununkhiza kodabwitsa kumandithandiza kupeza zipatso zakupsa komanso zokonzeka kudyedwa. Ndili ndi mano akuthwa oluma pakhungu lolimba la zipatso zina. Zitosi zanga zimathandiza kufalitsa miyala ndi mipopi ya zipatso kuti mitengo yazipatso ikule m'malo atsopano.

Mileme ina imadya timadzi tokoma m'maluwa n'kuitulutsa mungu ngati njuchi! Mileme imathandiza kutulutsa mungu ku zomera zosiyanasiyana zoposa 500, kuphatikizapo mango ndi nthochi. Pollination ndi kusamutsa mungu kuchokera ku chomera chimodzi kupita ku china kuti mbewu zatsopano zipangidwe. Popeza zomera sizingasunthike kuti zipeze zomera zina zoti zizitha kudulira mungu, zina zimadalira nyama monga mileme kuti ziziwathandiza. Mleme umawulukira ku chomera kukamwa timadzi tokoma kuchokera ku maluwawo. Pomwe mungu umamatirira kutsitsi la thupi lawo. Kenako mleme umaulukira ku chomera china kukapeza chakudya chowonjezereka, ndipo munguwo umasamutsidwa kuchoka m'thupi la mileme kupita ku chomera chatsopanocho!

ndowe ya mileme
Lero, mitengo
yazipatso mawa!



mmm chabwino chabwino!



Zomera zina za mileme zili ndi njira zanzeru zokokera mileme. Amakonda kutulutsa maluwa usiku (osati masana) kuti akope mileme yodyetsera usiku, amakhala ndi maluwa akuluakulu owoneka bwino kuti mileme ikhale yosavuta kupeza shuga mkati mwake, ndipo imakhala ndi fungo lamphamvu lomwe limatha kununkhiza. kwa inu anthu koma fungo lokoma kwa ife mileme. Ndipo mileme yomwe imadya timadzi tokoma imasinthidwanso mwapadera, imakhala ndi fungo lamphamvu ndipo ina imakhala ndi malilime aatali omwe amathandiza kuyamwa timadzi tokoma!

Mwinamwake mwamvapo za mileme yomwe imadya magari? Mileme yomwe imadya magari, imatchedwa mileme yachivapaya. Koma mumadziwa kuti pali mitundu itatu yokha ya mileme yachi vapaya ndipo onse amapezekela ku Central ndi South America. Tilibe mileme yachoncho kuno kummwera kwa Africa (kapena kulikonse mu Africa).



Ngakhale tilibe mileme yachi vapaya kum'mwera kwa Africa, timakonda mileme yachi vapaya! Mileme yachi vapaya si yowopsya ndipo siikonda kumwa magari aanthu. Pali mitundu itatu yokha (mitundu) ya mileme yachi vapaya padziko lapansi! Imakonda kumwa magari a mbalame komanso zimathanso kudya magari a nkumba, ng'ombe ndi akavalo. Amangomwa magari ochepa kwambiri, pafupifupi ma supuni a tiyi awiri, kotero nyama zambiri sizimazindikira nkomwe kuti mleme wayamwa magari!




Ntchito 2:

Nthawi ya chakudya chamadzulo!

Fananizani mawonekedwe a mileme ndi mtundu wa chakudya chomwe amadya - pali mfundo zokuthandizani kuti muchite izi!

Ndili ndi maso akulu komanso mphuno yayitali

Wodya tizilombo



Ndili ndi lilime lalitali komanso ndimanunkhiza bwino

Wodya zipatso



Ndine wamng'ono ndipo ndimagwiritsa ntchito ekolokeshoni kuti ndipeze chakudya changa

Wodya timadzi toshuga m'maluwa



2

Ekolokeshoni

Mileme siya khungu! Imatha kuwona bwino, koma mileme yomwe imadya tizilombo tating'ono mumdima imafunikira thandizo lina kuti igwire tizilombo timene imadya.


Imagwiritsa ntchito njira yotchedwa "ekolokeshoni" yomwe amafuula usiku wonse ndikumamvetsera kulira kwa mawu ndi makutu awo atcheru kuti adziwe pomwe tizilimbo tili. Komanso mileme ina imakhala ndi makutu akuluakulu omwe amawathandiza kumvesela tizilombo usiku!

Thandizeni!



Mwina mungaganize kuti mileme yambiri ikamafuula usiku imachita phokoso kwambiri ndipo mungadabwe kuti n'chifukwa chiyani simunaimvepo - koma phokoso limeneli n'lamphamvu kwambiri loti anthu sangalimve. Komabe anthu amatha kugwiritsa ntchito chida chotchedwa ditekita ya mleme kuti amvetsera zomwe mileme imachita usiku. Makina amenewa amatithandiza kumvetsera kulira kwa mileme, ndipo popeza mileme iliyonse ili ndi mawu ake osiyana ndi ena, timatha kudziwa mtundu wa mileme yomwe tikumvetsera.

Kwa inu!



Ntchito 3: Masewera a mileme ndi njenjete

Sewerani masewera a mileme ndi njenjete ndi anzanu kapena abale anu kuti mumvetsetse momwe mileme imagwiritsira ntchito ekolokeshoni kuti ipeze chakudya chawo, tizilombo (njenjete)!

Mufunika zotchinga m'maso ziwiri monga mpango ndi anthu ena osachepera awiri oti musewere nawo masewerawa.

- Sankhani munthu m'modzi kukhala mleme ndipo m'modzi akhale njenjete. Anthu awiriwa amavala zotchinga m'maso - tsopano ali "mumdimba".
- Ena onse amaima mozungulira mozungulira mileme ndi njenjete. Ntchito yawo ndikuteteza mileme ndi njenjete kuti asachoke mubwalo.
- Mleme umaitana kuti "mleme" ndipo njenjete imayankha kuti "njenjete". Onse ndiye kutenga sitepe.
- Mleme kapena njenjete zikafika m'mpheapete mwa bwalo anthuwo aziletsa pang'onopang'ono. Lamulo lofunika kwambiri ndiloti mileme ikayitana njenjete iyenera kuyankha.
- Mleme uyenera kuyesa kugwira njenjete, ndipo njenjeteyo iyenera kuyesetsa "kuwulukira" kutali ndi mileme.
- Tembukurirani kukhala mileme ndikuwona kutalika kwa mleme uliwonse kuti ugwire njenjete!



3

Mileme ya Kum'mwera kwa Africa

Tsopano popeza tadziwa zimene mileme imadya m'madera osiyanasiyana padziko pano, tiyeni tione zimene anzanga kuno kum'mwera kwa Africa amadya.



Bongi mleme wa makutu atali aku Botswana



Bebe Logan

Ndidakali wamng'ono kwambiri moti sindingathe kuwuluka ndi kugwira tizilombo. Chakudya changa ndi mkaka wa amayi anga

Ndimatha kugwira tizilombo tikamauluka kapena kutola tomwe tili pamasamba. Mapiko anga aakulu amandithandiza kuuluka pamene makutu anga Aakulu amamvetsera mosamalitsa phokoso la tizilombo tomwe tikuyenda pamasamba. Ndimatha kugwira tizilombo ndi mapazi anga n'kumapinda mchira wanga kuti tizilomboto nditigwire bwino. Ngati ndichilombo chachikulu kwambiri ndimakaimila pamalo enaake kumadya ndikulendewera m'malo mokudya pamene ndikuuluka.

Ine ndine Ashinga (Mleme Wolimba Mtima). Ndimatha kuwuluka pansi kwambiri ndi kukagwira kafadala pansi. Ndimauluka pang'onopang'ono komanso mosamala ndipo ndimadyera pakati pa masamba ndi nthambi. Mapiko anga aakulu amandipangitsa kuti ndizitha kuwongolera kwambiri koma sindikwanitsa kuwuluka mwachangu. Mano anga ndi akuthwa chifukwa chake ndimatha kuluma mapiko amphamvu a kafadala.




Mleme waku Egypt wong'ambika ndi Nycteris thebaica

Avnaya, Vampire Wonyenga, Lavia frons



Ndimagwira tizilombo tokulilapo. Ndimakonda kutchera khutu ndikumvetsera mwatcheru kuti ndimve kachiolombo komwe ndikufuna kudya, ndikangomva ndimalumpha! ndikukagwira! Makutu anga aakulu amasuthasutha ndi kumatembenuka, kumamvetsera komwe mawu akuchokera.

Ntchito 4: Zipewa za mileme



Pangani luso ndi anzanu ndikupanga zipewa zokhala ndi zibangili za mileme!

Zomwe mungafune (pa chipewa chilichonse cha mileme):

- Chidutswa chimodzi cha khadi kapena pepala lolimba pafupifupi 65cm kotalika ndi 3cm mulifupi - gulu lalikulu
- Mapepala awiri pafupifupi 30cm m'litali ndi 1cm mulifupi
- Mileme iwiri yamapepala, iduleni ndikuyikamo (pangani zopanga) kapena iduleni papepala lakuda

Mukadula gulu lanu lalikulu (bandi lakumutu), mutha kulikongoletsa ndikulipanga kuti ligwirizane ndi mutu wanu (mungagwiritsenso ntchito cellotape).



Lumikizani mileme kumapeto kumodzi kwa mapepala afupiafupi, kenaka tsatirani mbali ina kumutu monga momwe zilili pansipa:



Malingaliro opangira:

Bwanji osayesa kupanga chipewa china cha mileme?

Mmalo mwa mileme iwiri, mungakonde kukhala ndi mileme yambiri kapena bwanji za mileme ndi njenjete? Kapena mleme wa zipatso ndi chipatso chokoma?

Bwanji osakhala ndi phwando la chipewa cha mileme?

Mutha kuyitanira anzanu ndikukhala ndi phwando la zipewa za mileme ndipo mwinanso kukhala ndi mpikisano ndikuwona yemwe angapange chipewa chaluso kwambiri!



Kafotokozedwe ka mawu (mawu omwe taphunzira lero!)

Ekolokeshoni - Njira yowonera ndi mawu. Ndizothandiza kwambiri ngati palibe kapena kuwala kochepe kwambiri. Mileme yambiri imachita izi (mileme yazipatso ndiyosiyana nayo). Maitanidwe apamwamba amapangidwa, kaya kudzera pakamwa kapena mphuno ya nyama. Mauthenga amene amabwerera amathandiza mileme "kuona" zimene zili patsogolo pake, ngati chinthu chikuyenda mwachitsanzo, tizilombo touluka, mleme umatha kudziwa kumene ukulowera komanso liwiro la kuuluka. Ma dolphin nawonso amachita izi, popeza pali kuwala kochepe pansi panyanja.

Inisekitivorusi - Nyama kapena zomera zomwe zimadya tizilombo.

Fulujivo - Nyama yodya zipatso (monga Eidolon)

Polineshoni - Kusamutsa mungu kuchokera ku duwa lina kupita ku lina. Zimenezi n'zofunika kwambiri kuti mbeu zisamere ndi kubereka mbewu zathanzi.



Ndikukhulupirira kuti mwaphunzira zambiri lero!

Tikuwonani sabata yamawa, kuti mudziwe zonse za makanda a mileme!

Musaiwale; mayankho azochitikazo apezeka patsamba la Facebook la Bats without Borders!